

**KAZYOZYO EXAMINATIONS BOARD****2021 PRIMARY SCHOOL PRE-MOCK EXAMINATION****CHICHEWA****(100 Marks)**

TIME Allowed: 2 h 15 mins

1:00 3:15pm

TSIKU \_\_\_\_\_

DZINA LANU: \_\_\_\_\_

DZINA LA SUKULU : \_\_\_\_\_

**MALANGIZO**

1. Pepala ili lili ndi magawo anayi:

Gawo A,B,C ndi D

2. Lembani dzina lanu pamwamba pa tsamba lino

3. Lembani nambala la mayeso pamwamba pa tsamba

lililonse

4. Lembani chimangilizo kapena kalata mu Gawo A

ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo B,C ndi D

5. Muchitebulo chili pambalilichi onetsani funso

lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi

lomwe lilikutsogolo kwake

6. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso

(invijireta)

<i>Question number</i>	<i>Chongani zomwe mwayankha</i>	<i>Muno musalembemo</i>	
1			
2			
3			
4			
5			
6-10			
11-15			
16-20			
21-25			
26-30			
31-33			
34-35			
36-38			
39-40			
41-45			

GAWO A ( Malikisi 30)

Langizo: yankhani fuso limodzi lokha mwa mafuso awiri ali m'musiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:  
MASEWEWERA A KUMUDZI KWATHU  
Mawazina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba:

- i. Dzina la masewera omwe amachitika kumudzi kwanu.
- ii. Komwe masewerawa amachitikira
- iii. Nyengo yomwe masewerawo amachitikira.

Ndime yachiwiri:

- i. Zinthu zomwe amagwilitsa ntchito pa masewerowo
- ii. Kufunika kwa masewerowo
- iii. Maguli a anthu omwe amachita masewerowo

Ndime yachitatu:

- i. Zomwe anthu akumudzi kwanu akuchita kuti masewerawo asaiwalike. (malikisi 30)
2. Lembani kalata kwa agogo anu yowadzuwitsa kuti mudzapita kukawachezera pa tchuti mukalembe mayeso anu a sitandade 8.

Ndime yoyamba :

- ii. Chilinga cha kalata yanu
- iii. Tsiku lomwe mudzapite kwa agogo anuko
- iv. Nthawi yomwe mudzakhale muli kutchuthiko.

Ndime yachiwiri:

- i. Yemwe mudzapite naye kutchuthuko
- ii. Zomwe mudzatenge popita kutchuthiko
- iii. Chisangalano chomwe mudzakhale nacho mukadzapita kutchuthiko

Ndime yachitatu:

- i. Zomwe mukuyembekezera kudzachita kutchuthiko. (30 malikisi)





## GAWO B ( malikisi 20)

## KUNVESA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafuso otsatirawo.

Madzi ndi moyo. Mawuwa amanenedwa chifukwa chakuti zolengedwa zambiri zimadalira madzi kuti zikhale ndi moyo. Anthu, Nyama, Mitengo ndi zolengedwa zina zimafuna madzi. Mwachitsanzo munthu akanva ludzu amamwa madzi. Chifukwa nthupi mwake mumafunika madzi. Choncho ndi bwino kumwa madzi a ukhondo pafupipafupi kuti tikhale ndi moyo wabwino. Akafuna kusamba, kuphika, kuchapa zovala kapena kutsuka ziwiya munthu amagwilitsa ntchito madzi.

Nyama ndi mbalame zonse zimafuna madzi kuti zikhale ndi moyo. Kumaiko komwe kuli chilala, nyama ndi mbalame zimafa chifukwa cha ludzu. Nsomba ndi zolengedwa zonse za m' madzi sizingakhale ndi moyo popanda madzi. Mbewu nazonso kuti zimele ndi kukula bwino zimafunika madzi, zikasowa madzi zimanyala ndikufa. Pamakampani opanga zinthu monga zakumwa, mankhwala ndi zinthu zosiyanasiyana amagwilitsa ntchito madzi.

Madzi amapezeka m'mitsinje, m'nyanja, mzitsime ndi mzithaphwi. Makono anthu ambiri amagwilitsa ntchito madzi a apamjigo ndi a pampopi. Tsono popeza madzi ndi moyo ndikofunika kusamalira kwambiri madziwa. Pali njira zambiri mmene tingasamaklire madzi kuti asamasowe. Zina mwa izo ndikusaduala mitengo m'mpheapete mwa mitsinje ndi Nyanja, kusataya zinyalala m'mitsinkje kapena m'nyanja chifukwa zimachititsa kuti madzi akhale oipa, njira ina yomwe tingasamaklire madzi akumwa ndithiramo mankhwala omwe amapha tizilombo toyambitsa matenda. Mankhwala timatcha kuti kulolini.

Tigwilitse ntchito makapu awiri pamene tikumwa madzi athu. Kapu yoyamba ndiyotungira madzi ndipo ina ndiyoti tithiremo madzi ndi kumwa. M'madera ena madzi amasowa nyengo yachilimwe popeza amauma. Kumalo oterewo mkofunika kukumba zitsime zakuya komanso kukhala ndi njira zokololera madzi kuti tidzawagwilitse ntchito akasowa. ( buku la ophunzira la sitandade 6)

Tsopano yankhani mafuso otsatirawa pa misère ili pansu pa funso lililonse.

- a. Mawu oti " madzi ndi moyo" amanenedwa chifukwa chiyani? \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ (malikisi 2)
- b. Perekani ubwino umodzi woti anthu azimwa madzi aukhondo.? \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ ( malikisi1)
- c. Ndi ntchito ziwiri ziti zomwe anthu amagwiritsa ntchito madzi?
  - I. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
  - II. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- d. Kodi mawu oti " chilala" akutanthauzanji nkhanayi? \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ ( malikisi 2)

- e. Perekena chinthu chimodzi chomwe makampani amapanga pogwilitsa ntchito madzi?  
\_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- f. N'chifukwa chiyani madzi otunga m'zithaphwi ndi mzitsime sakhala abwino kumwa?  
\_\_\_\_\_ ( malikisi 2)
- g. Ndi njira ziwiri ziti zomwe tingasamalire madzi a m'mitsinje?  
I. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)  
II. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- h. Perekani mawu ofanana m'matathauzo ndi awa :  
I. Utchisi \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)  
II. Yachilimwe \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)  
III. Makono \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- i. Kodi ndimankhwala anji omwe angathe kuthiridwa m'madzi kuti tiphe tizilombo?  
\_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- j. Perekani ntchito ziwiri za makapu omwe timagwiritsa ntchito tikamamwa madzi.  
I. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)  
II. \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- k. Perekani mutu wankhaniyi. \_\_\_\_\_ ( malikisi 2)

4. GAWO C ( malikisi 10)

Yankhani mafuso onse awiri m'gawoli.

Welengani kankhanika ndipo muyankhe mafuso otysatirawo:

" Pepani anthu nonse mwafika pano. Tsopano ndi nthawi yoti tiyamba mwambo woperekeza mfumu yathu yagona apayi."

- I. Kodi malonje angaperekedwe pamwambo wanji? \_\_\_\_\_  
(malikisi 1)
- II. Lembani udindo wa munthu amene angapereke malonjewa. \_\_\_\_\_  
( malikisi 1)
- III. Kodi mawu oti "mfumu " akutathauzanji? \_\_\_\_\_ (malikisi 1)
- IV. Perekani njira ziwiri zomwe tingasamalire odwala chifukwa chachikulu. \_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_  
\_\_\_\_\_ ( malikisi 2)

5. Kupanga ziganizo:

Pangani ziganizo zonzeka bwino ndi mawu awa:

- I. Kudwala \_\_\_\_\_ (malikisi 1)
- II. Ngati \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- III. Phwete \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)
- IV. Pa \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)

## V. Njenjemera \_\_\_\_\_ ( malikisi 1)

GAWO D ( malikisi 40)

Zungulizani limbo lokhoza ( A,B,C kapena D)  
m' mafuso otsatirawa:Mafuso 6 mpaka 10 sankhani mitundu ya  
mawu omwe atsekedwa mzere kungsi  
kwawo m' ziganizo zotsatirazi:

6. Ophunzira okonda kujomba  
amalephela mayeso.  
(A) Mfotokozi  
(B) Dzina  
(C) Mneni  
(D) Mlowam' malo
7. Ubwereke njinga ziwiri kuti tiyende  
bwino  
(A) Mlowam' malo  
(B) Muonjezi  
(C) Mfotokozi  
(D) Dzina
8. Iye ndi mphunzitsi.  
(A) Mneni  
(B) Mlowam' malo  
(C) Muonjezi  
(D) Mlumikizi
9. Awa apambana mayeso  
(A) Muonjezi  
(B) Mvekero  
(C) Mlowam' malo  
(D) Mfuwu
10. Mtolo wankhuni uli ndi  
(A) Muonjezi  
(B) Mvekero  
(C) Mlowam' malo  
(D) Mfuwu

Mafuso 11 mpaka 15: sankhani mitundu ya  
afotokozi omwe ali ndi mzere kungsi kwawo  
m' ziganizo zotsatirazi:

11. Undibwereke buku lililonse  
(A) Woloza  
(B) Wopatula  
(C) Waumwini  
(D) Wa mgwirizano
12. Iye wavala Malaya otuwa  
(A) Wa makhalidwe  
(B) Wa umwini  
(C) Woloza  
(D) Wa maonekedwe
13. Wagula mbuzi zinayi  
(A) Wa maonekedwe  
(B) Woloza  
(C) Wa amwerengero  
(D) Wopatula
14. Galu wolusa uja waphedwa  
(A) Wopatula  
(B) Wa maonekedwe  
(C) Wa makhalidwe  
(D) Woloza
15. Zinthu zomwe amafuna wazipeza.  
(A) Wa umwini  
(B) Wa mgwilizano  
(C) Wa maonekedwe  
(D) Woloza.

Mafuso 16 mpaka 20: sankhani mayina  
omwe ali m' mitundu yotsatirayi.:

16. Dzina lamwinimwini  
(A) Mtungo  
(B) Bamboo  
(C) Zomba  
(D) Sukulu

17. Dzina la unyinji  
 (A) Uve  
 (B) phavu  
 (C) Anyamata  
 (D) malingaliro
18. Dzina lopanda la umwinimwini  
 (A) Ulesi  
 (B) Mulu  
 (C) Shire  
 (D) Nyakwawa
19. Dzina la chithu chosakhudzika  
 (A) Mbatata  
 (B) Malovu  
 (C) Tsoka  
 (D) munthu
20. dzina la chinthu chokhudzika  
 (A) Ulemu  
 (B) Mpando  
 (C) Msambi  
 (D) Mlengalenga

Mafuso 21 mpaka 25: sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe atsekedwa mzele kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

21. Kapu yanga idasweka  
 (A) Wom'chitira  
 (B) Wochitirana  
 (C) Wochititsa  
 (D) Wochitidwa
22. Agogo awaphikira chakudya  
 (A) Wochititsa  
 (B) Wom'chitira  
 (C) Wochitirana  
 (D) Wochitidwa
23. Njinga zija zawombana  
 (A) Wochititsitsa  
 (B) Wochitidwa  
 (C) Wochitirana

- (D) Wochititsa
24. Awa amagonagona  
 (A) Wochititsitsa  
 (B) Wobwerezabwereza  
 (C) Wotsutsa  
 (D) Wochitidwa
25. Iye wamasula thumba  
 (A) Wom'chitira  
 (B) Wochititsa  
 (C) Wochitidwa  
 (D) Wotsutsa

Mafuso 26 mpaka30: sankhani ntchito za m'ziganizo zotsatirazi.

26. Abambo agula nyumba  
 (A) Dzina loitanira  
 (B) Mtsilizitsi wa mneni  
 (C) Mwininkhani  
 (D) Pantherankhani
27. Aphunzitsi akuphunsitsa  
 (A) Dzina lapadera  
 (B) Mwininkhani  
 (C) Pantgherankhani  
 (D) Dzina loitanira
28. Malita, pita ku msika  
 (A) Dzina loitanira  
 (B) Mwininkhani  
 (C) Pantherankhani  
 (D) Mtsilizitsi wa mneni
29. Bambowa ndi mbiyang'ambi  
 (A) Mtsilizitsi wa mneni  
 (B) Dzina lapadera  
 (C) Panthelankhani  
 (D) Dzina loitanira
30. Zuze, chilombo wabwera  
 (A) Dzina loitanira  
 (B) Dzina lapadera  
 (C) Pantherankhani



(D) Mwininkhani

Mafuso 31 mpaka 33: sankhani mitundu nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

31. Malesa adakwa ndi aphiri

- (A) Yakale yopitilira
- (B) Yakale yathayi
- (C) Yakale
- (D) Yakale yakawirikawiri

32. Takhala tikuyimba ndi anzathu

- (A) Yatsopano yopitilira
- (B) Yatsopano
- (C) Yatsopano yakawirikawiri
- (D) Yatsogolo

33. Tidzalemba mayeso mwezi wamawa

- (A) Yatsogolo yopitiriza
- (B) Yatsogolo
- (C) Yatsopano
- (D) Yatsipano yopitiriza

Mafuso 34 mpaka 35: sankhani chichikazi pamayina otsatirawa.

34. Mfumu

- (A) Namkungwi
- (B) Mfumukazi
- (C) Chemwali
- (D) Mfumakazi

35. Phungu

- (A) Mpongozi
- (B) Zakhali
- (C) Namkungwi
- (D) Mfumakazi

Mafuso 36 mpaka 38: sankhani mikuluwiko yomwe ikutsutsana m' matantghauzo ndi yomwe mwapatsidwayi.

36. Kuchulukana ndikwabwino kuipira kuthetsa sunzi m' mbale.

- (A) Pawiripawiri sipawuzirika
- (B) Njuchi zikachuluka siziyika uchi
- (C) Mutu umodzi siyuseza denga
- (D) Tili tiwiri n'tianthu kali kokha n'kanyama

37. Mwana wamzako ndiwako yemwe ukachenjera manja udyo naye.

- (A) Mutu umodzi sisenza denga
- (B) Fodya wako ndi uyo ali pamphuno
- (C) Mwana wamwini ndi gaga sakundika
- (D) Ali dere mkulinga utayenda naye

38. Ukayendera mzengo usamati asakhwi afumbula.

- (A) Pakadafunda padajiwitsa galu
- (B) Ukayenda m'tchire wayendera zonse
- (C) Zengerezu adalinda kwawukwawu
- (D) Ichi m'chiyani mkulinga muli awili

Mafuso 39 mpaka 40: sankhani magulu amayina ojmwe atsekedwa nzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

39. Ndege yafika nthawi yabwino

- (A) U-,ma-
- (B) I-,zi-
- (C) Chi-,zi-
- (D) Mu-,a-

40. Ukapereke chakudya kugowero

- (A) Chi-,zi-
- (B) Ka-,ti-
- (C) Mu-,a-
- (D) I-,zi-

Mafuso 41 mpaka 45; sankhani mitundu ya nthambi zomwe za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

41. Ophinzira omwe azakhoze bwino  
adzawasankhira ku sekondale.

- (A) Ya mfotokozi
- (B) Yoyima payokha
- (C) Ya muonjezi
- (D) Ya dzina

42. Mvura ivuta kubwera chifukwa  
tadula mitengo yonse

- (A) Yadzina
- (B) Ya mfotokozi
- (C) Yoyima payokha
- (D) Ya muonjezi

43. Zoti Nyanja yathu ikuphwa ndizoona

- (A) Ya mumuonjezi
- (B) Yoyima payokha

(C) Ya mfotokozi

(D) Ya dzina

44. Mnyamata amene wakhala apoyo  
ndi wakuba

- (A) Yoyima payokha
- (B) Ya dzina
- (C) Ya mfotokozi
- (D) Ya muonjezi

45. Udzapambana pokhapokha  
ukadzalimbikira

- (A) Ya muonjezi
- (B) Yoyima payokha
- (C) Ya mfotokozi
- (D) Ya dzina

MAFUNSO ATHERA APA!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!!